

THE QUEBEC DECLARATION ON LITERARY TRANSLATION AND TRANSLATORS

(Chichewa Version)

KULENGEZA CHIMANGO CHA KU QUEBEC ZA KUTANTHAUZIRA NDI OTANTHAUZIRA

1. Kutanthauzira zolemba ndi luso lamtengo wapatali ndi lopatsa chidwi. Kutanthauzira kumabweretsa kupambana kwa kumasukirana, kumathandiziranso kubweretsa mtendere ndi ufulu polimbana ndi kusalungama kwa zigamulo ndi kusowa kwa kulolerana pamchitidwe wosefa zolembedwa. Koposaposa, kutanthauzira kumalimbikitsa ku kukambirana kwaphindu kwa onse padziko lapansi.
2. Tikamakamba zo tanthauzira, chikhalidwe chilichonse chimakhala chosiyana ndi chinzake. Magulu ena amatanthauzira mwa kufuna kwao pamene magulu ena amatanthauzira pakukakamizidwa kuti atero kapena kuwona kuti ndikofunika kutero. Kutanthauzira kumatsegula njira zotetezera zilankhulo ndi chikhalidwe za wanthu.
3. Popanda kunyozetsa opeka ndi zolemba zawo, otanthauzira alinso ndi luso lawo lawo mwa iwo okha. Sikuti amangofuna kubwereza zomwe alemba anthu aluso ena koma kupititsa patsogolo, kuti zifikire anthu ochuluka. Otanthauzira si atumwi chabe: ngakhale amayankhula za ena, koma mawu omvekawo amakhala aiwo eni. Makamaka amathandizira kupambana kwa chikhalidwe chosiyana-siyana potumikira mokhulupirika olemba, zolembedwa, kalembedwe kosilirika ndikukweza magulu a anthu omwe samalabadirika ndi kale lonse.
4. Ufulu wa otanthauzira utetezedwe . Maboma, osindikiza mabukhu, mabungwe ndi nyumba zoulutsa mau ndi kufalitsa nkhani, olemba ntchito, onsewa alemekeze udindo wa otanthauzira ndikulemekeza magwiridwe awo antchito.
5. Anthu otanthauzira nawonso atetezedwe ngati momwe amatetezedwera wolemba wina ali yense.
6. Ngati anthu a luso la iwo okha, ndi nzeru zapadera, otanthauzira akuyenera kulemekezedwa ndipo kupatsidwa mwai woyankha mafunso aliwonse wokhudzana ndi ntchito yomwe ayigwira. Ntchito za anthu otanthauzira zitengedwe kuti ndi luso la iwo amene azitanthauzirawo kuti aliyense asziwike pantchito yake.